Food and Agriculture Organization of the United Nations

Ndondomeko Zosakakamiza Zolimbikitsa Ntchito Zing'onozing'ono Za Usodzi Zokhalitsa

Mogwirizana ndi Ntchito Yowonetsetsa kuti Anthu ali ndi Chakudya Chokwanira ndi Kuthetsa Umphawi



Ndondomeko Zosakakamiza Zolimbikitsa Ntchito Zing'onozing'ono Za Usodzi Zokhalitsa

Mogwirizana ndi Ntchito Yowonetsetsa kuti Anthu ali ndi Chakudya Chokwanira ndi Kuthetsa Umphawi

Food and Agriculture Organization of the United Nations
Rome, 2022

Required citation:

FAO. 2022. *Ndondomeko Zosakakamiza Zolimbikitsa Ntchito Zing'onozing'ono Za Usodzi Zokhalitsa - Mogwirizana ndi Ntchito Yowonetsetsa kuti Anthu ali ndi Chakudya Chokwanira ndi Kuthetsa Umphawi*. Rome. https://doi.org/10.4060/i4356ny

The designations employed and the presentation of material in this information product do not imply the expression of any opinion whatsoever on the part of the Food and Agriculture Organization of the United Nations (FAO) concerning the legal or development status of any country, territory, city or area or of its authorities, or concerning the delimitation of its frontiers or boundaries. The mention of specific companies or products of manufacturers, whether or not these have been patented, does not imply that these have been endorsed or recommended by FAO in preference to others of a similar nature that are not mentioned.

ISBN 978-92-5-135848-1

© FAO, 2022

© FAO, 2015 [English edition]

Some rights reserved. This work is made available under the Creative Commons Attribution-NonCommercial-ShareAlike 3.0 IGO licence (CC BY-NC-SA 3.0 IGO; https://creativecommons.org/licenses/by-nc-sa/3.0/igo/legalcode).

Under the terms of this licence, this work may be copied, redistributed and adapted for non-commercial purposes, provided that the work is appropriately cited. In any use of this work, there should be no suggestion that FAO endorses any specific organization, products or services. The use of the FAO logo is not permitted. If the work is adapted, then it must be licensed under the same or equivalent Creative Commons licence. If a translation of this work is created, it must include the following disclaimer along with the required citation: "This translation was not created by the Food and Agriculture Organization of the United Nations (FAO). FAO is not responsible for the content or accuracy of this translation. The original [Language] edition shall be the authoritative edition."

Disputes arising under the licence that cannot be settled amicably will be resolved by mediation and arbitration as described in Article 8 of the licence except as otherwise provided herein. The applicable mediation rules will be the mediation rules of the World Intellectual Property Organization http://www.wipo.int/amc/en/mediation/rules and any arbitration will be conducted in accordance with the Arbitration Rules of the United Nations Commission on International Trade Law (UNCITRAL).

Third-party materials. Users wishing to reuse material from this work that is attributed to a third party, such as tables, figures or images, are responsible for determining whether permission is needed for that reuse and for obtaining permission from the copyright holder. The risk of claims resulting from infringement of any third-party-owned component in the work rests solely with the user.

Sales, rights and licensing. FAO information products are available on the FAO website (www.fao.org/publications) and can be purchased through publications-sales@fao.org. Requests for commercial use should be submitted via: www.fao.org/contact-us/licence-request. Queries regarding rights and licensing should be submitted to: copyright@fao.org.

Bukuli linalembedwa polemekeza a Chadrika Sharma
amene anagwira ntchito modzipereka pofuna
kukweza miyoyo ya anthu ogwira ntchito
zokhudza nsomba padziko lonse lapansi
ndipo anatenga gawo lalikulu polemba ndondomekozi

Mawu Oyamba

Ndondomeko zosakakamiza zolimbikitsa ntchito zing'onozing'ono za usodzi zokhalitsa zokonzedwa mogwirizana ndi ntchito yowonetsetsa kuti anthu ali ndi chakudya ndi kuthetsa umphawi ndi mfundo zoyamba padziko lonse zomwe cholinga chake ndi kuyang'anira nthambi ya ntchito zing'onozing'ono za usodzi yomwe kwa nthawi yaitali yakhala ikupatsidwa chidwi chochepa.

Gawo la ntchito zing'onozing'ono za usodzi limakhala lokhazikika kwambiri ku madera komwe asodzi ang'onoang'ono amakhala, pachikhalidwe ndi maganizidwe omwe anthu akuderako amakhulupilira kuti zimawaluzanitsa pamodzi. Asodzi ang'onoang'ono ambiri amadzilemba ntchito okha komanso amapezeka ndi nsomba zomwe zimagwiritsidwa ntchito m'makomo komanso m'madera awo. Amayi amatengapo mbali yofunikira m'gawo limeneli maka pakasamalidwe ka nsomba zisanafike kumsika. Pafupifupi anthu 90 mwa 100 aliwonse omwe amagwira ntchito za usodzi polembedwa ntchito m'magawo a ntchito zing'nozing'gono za usodzi. Choncho, ntchito zing'onozing'nozi zimathandiza ku gawo la chuma komanso kuchengetera miyoyo powonesetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira chomanga matupi awo, mwayi wa ntchito ndi zinthu zina zobweretsa chuma kumadera amene amadalira usodzi.

Ndondomeko zosakakamizazi zakhazikitsidwa mochedwerapo chifukwa cha kusoweka kwa mfundo zosindikizidwa zovomerezeka ndi dziko lonse zothandizira kuti pakhale kufanana pakaperekedwe ka upangiri oyenera pantchito zing'onozing'no za usodzi. Ndondomekozi zikuthandizira malamulo okhudza kagwiritsidwe ntchito kabwino kaza usodzi mogwirizana ndi mfundo zoyendetsera usodzi zomwe m'malamulo a Bungwe la Umodzi pa Dziko Lonse (United Nations) okhudza nyanja. Ndondomeko zosakakamizazi ndi zofanana ndi ndondomeko zina za mtundu omwewu pakagwiritsidwe ntchito koyenera kamalo, malo ochitira usodzi ndi nkhalango powonetsetsa kuti chakudya chikupezeka chokwanira, komanso anthu ali ndi ufulu wokhala ndi chakudya chokwanira nthawi zonse. Mfundo zowonesetsera kuti ndalama zokwanira zikuperekedwa ku ntchito zotukula ulimi ndi kapezekedwe kachakudya. Ndondomeko zosakakamizazi zaika chidwi chachikulu pa ma ufulu a anthu komanso kuonetsetsa kuti zosowa za magulu a anthu omwe miyoyo yawo nthawi zambiri imakhala paziospyezo zosiyanasiyana ndi oponderezedwa zakwaniritsidwa.

Ndondomeko zosakakamizazi zakonzedwa pogwiritsa ntchito dongosolo lofuna kuti anthu onse okhudzidwa ndi zochitikazi akutenga nawo gawo potsatira zokambirana zamsonkhano wa 29 ndi 30 wa Komiti ya FAO pa ntchito za usodzi (COFI). Pakati pa chaka cha 2010 ndi 2013, bungwe la FAO linatsogolera kafukuku amene anakhudza nthumwi zosachepera 4,000 zamayiko, asodzi ang'onoang'ono, mabungwe ndi onse ogwira ntchito za usodzi , akafukufuku, mabungwe othandiza pachitukuko ndi magulu ena okhudzidwa ochokera m'mayiko oposera 120 m'zigawo 6 komanso misonkhano yosachepera 20 yotsogozedwa ndi mabungwe aboma yofunsa maganizo a anthu. Zotsatira zamisonkhano imeneyi zinapereka maziko a ntchito ya FAO yofunsa maganizo a anthu okhudzidwa, pamkumano wa m'mwezi wa Meyi 2013, ndi Febuluwale 2014 ofuna kugwirizana mfundo zolembera bukuli. Kuvomerezedwa kwa ndondomeko zosakakamiza ndi msonkhano wa COFI pa 31 Juni 2014 kukuimira chipambano chachikulu poonetsetsa kuti ntchito zingo'nozing'ono za usodzi zikukhala zodalirika nthawi zonse.

Ndondomeko zosakakamizazi ndi chida chofunikira pokwaniritsa masomphenya a bungwe la FAO ofuna kuthetsa njala ndi kulimbikitsa chitukuko monga momwe zinalembedwera m'ndondomeko zatsopano za kagwiridwe kantchito kabungweli. Mfundozi zitsogolera mu zokambirana, ntchito yopanga ndondomeko zoyendetsera ntchito zosiyanasiyana ndi zoyenera kuchita m'njira zosiyanasiyana ndi kuthandiza gawo la ntchito zokhudza nsomba kukwaniritsa ntchito yoonetsetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira komanso yothetsa umphawi. Chomwe chatsala tsopano ndikuti mamembala a bungwe la FAO komanso ena onse okhudzidwa agwiritse ntchito ndondomekozi mmagawo osiyanasiyana antchito zawo.

Pantchito yolimbikitsa kuti pakhale ntchito zing'onozing'ono za usodzi zokhalitsa mogwirizana ndi ntchito yowonesetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira ndi yothetsa umphawiyi, bungwe la FAO ndilodzipereka kuwonesetsa kuti ndondomeko zosakakamizazi zikugwiritsidwa ntchito ndikuti pali kulumikizana pakati pa bungweli ndi mabungwe onse okhudzidwa monga mayiko, asodzi ang'onoang'ono, ogwira ntchito zokhudza nsomba ndi mabungwe awo, mabungwe aboma, ochita kafukufuku ndi aphunzitsi msukulu zaukachenjede, ochita malonda, za mafakitale, mabungwe ndi mayiko othandiza pachitukuko.

José Graziano da Silva
Former FAO Director-General

Za M'katimu

Zolinga za Bukuli. IX

Loyamba

Mawu Otsogolera 1

1. Zolinga 1
2. M'mene ndondomekozi zilili 1
3. Mfundo Zotsogolera 2
4. Kulumikizana pakati pa ndondomekozi ndi mfundo zam'mayiko osiyanasiyana 5

Gawo Lachiwiri

Ntchito za usodzi Zogwiridwa moyenera 7

5. Kayendetsedwe ka umwini wa malo ndi zinthu zina mu ntchito zing'onozong'ono za usodzi ndi kagwiritsidwe ntchito koyenera ka zinthu. 7
    5a Kayendetsedwe koyenera ka umwini wa malo 7
    5b. Kusamala zinthu zamoyo za m'madzi moyenera 9
7. Kukonza nsomba zisanapite ku malonda 14
8. Kusasiyanitsa kagwiridwe kantchito pakati pa amuna ndi akazi 16
9. Ziwopsezo za ngozi ndi kusintha kwanyengo 17

Gawo Lachitatu

Kuonetsetsa kuti zochitika kukwaniritsidwa mwachikonzero 20

10. Kumveka bwino kwa ndondomeko,mogwirizana ndi kugwilira ntchito limodzi kwa mabungwe 20
11. Kufalitsa mauthenga, zotsatira zakafukufuku ndi kulumikizana 21
12. Kupereka upangiri 23
13. Thandizo pokwaniritsa ndondomeko ndi kulondoloza kakwaniritsidwe kake 24

Mawu Otsogolera

Matanthauzo a mawu olembedwa mwachidule

CCA
Kusintha Machitidwe Azinthu Mogwirizana ndi Kusintha kwa Nyengo

CEDAW
Mfundo Zothetseratu Kasalidwa kwa Amayi kwa Mtundu uli Wonse

CSO
Bungwe Lomenyera ndi Kulimbikitsa Ufulu Wachibadwidwe

DRM
Ntchito Yokhudza Kupewa ndi Kuchpetsa Mavuto Ogwa Mwadzidzidzi

EAF
Njira Zogwilira Ntchito Zokhudza Nsomba Moganizira Zachilengedwe Zokhala Modalirana Zokhudza Nsomba

HIV/AIDS
Kachilombo Koyambitsa matenda a Edzi

ICESCR
Pangano la Pakati pa Maiyiko pa hani za Ufulu wokhudza Chuma, Kakhalidwe ka anthu ndi Chikhalidwe

IGO
Bungwe la Pakati pa Maiko

ILO
Bungwe Lowona za Ntchito pa Dziko Lonse

IMO
Bungwe Loona za Nyanja pa Dziko Lonse

IUU
Usodzi Osavomereka, Osadziwika, ì ndi Ozembera Malamulo

MCS
Kuwonesetsa Kakaniritsidwe Kachikonzero, Kupewa Chisawawa ndi Kuponya Maso Pazochitika

NGO
Bungwe Lomwe Silaboma

RIO+20
Msokhano Wa Bungwe la. M'gwirizano pa Dziko Lonse Pa Chitukuko Chokhalitsa

THE CODE
Nfundo Zoonetsera Kuti Ntchito Zokhudza Nsomba Zikugwiridwa ndi Njira Zabwino

UN
Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko pa Dziko Lonse

UN DRIP
Mfundo za Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko pa Dziko Lonse Zokhudza Ufulu wa Wachibadwidwe wa Anthu

UNFCCC
Ndondomeko za Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko pa Dziko Lonse pa Nkhani ya Kusintha kwa Nyengo

WTO
Omwe Amakhala M'malo Achibadwidwe a mtundu wawo

Zolinga za Bukuli

Ndondomeko zosakakamiza zolimbikitsa ntchito zing'onozing'ono za usodzi okhazikika zopangidwa polingalira ntchito yothetsa umphawi ndi kuonetsetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira zakhazikitsidwa kuti zithandizire mfundo zabungwe la FAO. Mfundozi zinakhazikitsidwa m'chaka cha 1995 pofuna kuonetsetsa kuti ntchito za usodzi zikugwiridwa mwadongosolo. Ndondomekozi zinakhazikitsidwa kutsogolera ntchito zing'onozong'ono za usodzi polemekeza malamulo akulu abungwe la FAO. Ndondomekozi zikuunikira, kuzindikira ndi kukulitsa ntchito zomwe zilipo kale zokhudza ntchito zingo'onzing'ono za usodzi komanso kuthandizira zochitika za m'mayiko ndi padziko lonse zokhudza kuthana ndi njala komanso umphawi. Ndondomekozi zimalimbikitsa ntchito za usodzi wabwino ndi chitukuko chokhalitsa pokhudza miyoyo ya anthu ndi chuma zomwe ndizopindulira m'badwo uno komanso yamtsogolo muno. Ndondomekozi zithandizira zochitika zokhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi ndi onse ogwira nchitozi komanso magawo a anthu amene nthawi zambiri satetezedwa, amasalidwa komanso kulimbikitsa maufulu osiyanasiyana wa anthu.

Ndondomekozi nzosakakamiza, zikuimilira maiko onse, komanso ndizokhazikika pazosowa za mayiko maka omwe akutukuka kumene.

Ntchito zing'onozing'ono ndi zaluso za usodzi ndi ulimi wansomba kuphatikizapo ntchito zobweretsa phindu musanakolole, pokolola ndi pamene kukolola kwatha, zogwiridwa ndi amayi ndi abambo, zimathandiza kuti anthu akhale ndi chakudya chokwanira ndi chothandiza matupi awo, komanso zimathandiza kuthetsa umphawi ndi kugwiritsa kagwiritsidwe kosamala ka zachilengedwe zam'madzi[1] kuti zisatheretu. Ntchito zing'onozing'ono za usodzi zimapereka zakudya zomanga thupi kugulitsidwa m'misika yam'madera, ndi m'mayiko akunja, zomwe zimabweretsa chuma ku anthu ndi maiko awo.

Ntchito zing'onozing'ono za usodzi zimatulutsa koposa theka la nsomba zonse zimene zimaphedwa padziko lonse.

Polingalira kuchuluka kwa nsomba zimene anthu amadya ndi , chiwerengero zomwe zimaphedwa kupyolera mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi ndi chochuluka ndi nsomba ziwiri pa zitatu zilizonse. Ntchito zing'onozing'ono za usodzi m'nyanja ndi madera akumtunda zimakhala zofunikira pamene nsomba zambiri zophedwa ndi asodzi ang'onoang'ono zimadyedwa. Anthu okwana 90 pa 100 aliwonse onse amagwira ntchito zokhudzana ndi usodzi ochitika mwapang'onopang'ono , ndipo theka laiwo ndi amayi. Kupatula kulemba anthu ntchito kusodza kopitiliza kapena kwa apo-ndi-apo zimapezetsa anthu zinthu zogwiritsa ntchito zoonjezera ndi zina zosoweka paumoyo wawo. Machitachita amenewa amatha kukhala akumbali chabe koma pena amatha kukhala ofunika kwambiri, makamaka munyengo yamavuto.

Asodzi ang'ono ang'ono ambiri pamodzi ndi anthu ena ogwira ntchito zina zokhudza nsomba amadzilemba okha ntchito ndipo amadzipereka kwambiri popezera chakudya maanja awo ndi madera awo, komanso amapha, kukonza ndi kukagulitsa okha nsombazo. Ma gawo a ntchito zonsezi zimalimbikitsa kapezedwe ka chuma m'makomo awo komanso madera omwe ali mphepete mwanyanja kotero zimathandizanso potukula chuma cha dziko.

Ntchito zing'onozing'ono za usodzi zimayimilira magawo azochitika m'moyo osiyanasiyana omwenso amasinthasintha mkupita kwa nthawi, ndipo nthawi zambiri ntchitozi zimagwiridwa ndi anthu oti amachoka kwawo kupita kumadera ena mu nyengo zoyikika. Zizindikiro zokhazikika zamagawowa zimasintha potengera malo; makamaka kumadera omwe zimachititsa kuti anthu maona kulumikizana kwa nsomba ndi moyo wawo kuphatikizapo zinthu zimene iwo amayikapo mtima pokhulupilira kuti zimenezo ndizo zimawamanga pamodzi. Asodzi ambiri ang'onoang'ono, usodzi umayimira chikhalidwe chokhuthala ndi chosiyanasiyana chomwe ndi chofunika padziko lonse.

1. Mubukuli mawu oti zamoyo zam'madzi akugwiriritsidwa ntchito ponena za zamoyo zonse za m'madzi zopezeka m'nyanja za mchere ndi zopanda mchere zomwe zimagwiridwa ndi kudyedwa ndi anthu.

Asodzi ambiri ang'onoang'ono, komanso anthu ena ogwira ntchito zokhudza nsomba, anthu ama'madera awo, kuphatikizapo magulu a anthu ovutika ndi oponderezedwa, amafunikira kuti aziloredwa kugwira nawo ntchito zausodzi komanso za ulimi. Ufulu okhala ndi malo mphepete mwa nyanja ndi m'malo ena mopezeka madzi ambiri ndiwofunika kwambiri pothandizira kuti asodzi ang'onoang'ono akhale ndi mwayi wogwiritsa ntchito malo omwe mumapezeka nsomba kuphatikizapo ntchito zothandizira usodzi monga kukonza ndi kugulitsa nsomba, komanso kukhala ndi nyumba ndi zonse zothandizira umoyo. Kuchita bwino kwa zinyama zamoyo ndi zomera zam'madzi zosiyanasiyana ndi kofunika kwambiri powonetsetsa kuti nsomba zipitilire kupezeka kotero zikathe kuthandiza chumandi umoyo wabwino wa anthu.

Izo zili apo, ambiri amene amatenga nawo mbali m'ntchito zing'onozing'ono za usodzi amasalidwa ndipo akuyenera kulimbikitsidwa powonetsetsa kuti akupeza nawo chakudya chofunikira mthupi, kuthetsa umphawi, chitukuko chokomera onse ndi kusamalira zachilengedwe mosaponderezedwa.

Kuteteza ndi kuchulukitsa thandizo lomwe ntchito zing'onozing'ono za usodzi limapereka kumakumana ndi mavuto angapo. M'zaka makumi atatu kapena anayi zapitazi, nthawi zambiri, ntchito zotukula gawo la usodzi padziko lonse zakhala zikuwonongetsa zinthu zomwe zimagwiritsidwa ntchito pofuna kupeza zosowa m'moyo ndipo zakhala zikupereka chiwopsyezo kwa malo okhala anthu, zinthu zina zamoyo ndi njira zimene chilengedwe chimakhalira modalirana.

Miyambo yogawira ndi yogawanirana zinthu zogwiritsa ntchito pakati pa asodzi ang'onoang'ono, zomwe zakhala zikugwiritsidwa ntchito kwanthawi yayitali, zinasinthidwa popeza anthu samatenga nawo gawo pazochitika komanso kamba kaulamuliro wopereka mphamvu zambiri kwa anthu otsogolera omwe ndi ochepa, kusintha kwa luso la sayansi m'nthawi yochepa. Komanso pkatipa pakhala kusintha kwakukulu kwa magulu osiyanasiyana a anthu. Anthu amene amatenga mbali m'ntchito zing'onozing'ono za usodzi ali ndi zosiyana pakati pawo zimene zadzetsanso mabvuto akusiyana maganizo pakati asodzi akuluakulu ndi ang'onoangono. Pamakhala kudelerana ndi kupikisana pantchito za usodzi ndi zochitika m'moyo wa tsiku ndi tsiku. Magawo enawa kawirikawiri amatha kukhala ndi mphamvu zambiri pandale chuma, ntchito zokopa alendo, ulimi wa nsomba, mbewu, migodi, zopanga katundu, zomangamanga ndi zina.

Pamene m'madera ambiri aza usodzi muli umphawi asodzi ang'onoang'ono amakhudzika kwambiri posakhala ndi zinthu zochepa zokha, komanso umawalepheretsa asodzi ang'onoang'onowa kudyelera ufulu wawo wachibadwidwe monga

okhudza umzika, ndale, chuma ndi chikhalidwe. Madera amene mumachitika ntchito za usodzi ung'onoung'ono nthawi zambiri amapezeka kutali ndi malo otukuka zimene zimawapangitsa asodzi ang'onoang'onowa kumakumana ndi mavuto ambiri akafuna kufikira misika, za umoyo ndi zinthu zina zosoweka pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Zina zodziwika bwino zokhudza malo amenewa ndi monga: anthu kukhala ndi maphunziro ochepa, kupezeka kwa kachilombo koyambitsa matenda a Edzi ndi matenda a Edzi amene, kusowekera kwa upangiri wabwino oyendetsera magulu ndi mabungwe. Mwayi omwe umapezeka umakhala ochepa, zomwe zimapangitsa kuti anthu amene amatenga mbali m'ntchito za usodzi ung'onoung'ono zizikumana ndi mavuto monga kuchepekedwa kwa zochita zina zopezera zosowa pa umoyo , ulova pakati pa achinyamata, kugwira ntchito m'malo osatetezedwa ndi oyika moyo pachiwopsyezo, kugwiritsidwa ntchito mokakamizidwa komanso kugwiritsa ntchito ana. Kuonongeka kwa malo ogwirilapo ntchito, kuonongeka kwa chilengedwe, zotsatira zakusintha kwanyengo, ngozi zogwa mwadzidzidzi kamba kakusakazika kwa zachilengedwe zimaonjezera mavuto m'madera omwe m'machitika ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Zinthu zonsezi zimapangitsa asodzi ang'onoang'ono ndi anthu ena ogwira ntchito za usodzi kulowelerapo poteteza maufulu awo achibadwidwe monga kukhala ndi malo, komanso kulimbikitsa kagwiridwe kabwino ka ntchito zoteteza zachilengedwe zinthu zomwe zimapomboneza usodzi okhazikikaNdondomekozi zakonzedwa pogwiritsa ntchito mfundo zolimbikitsa anthu kutenga nawo mbali pazokambirana zotukula usodzi ung'onoung'ono pakati pa iwo ndi mabungwe owona za ufulu wa anthu, nthambi zaboma , mabungwe oyimilira zigawo za maiko ndi ena okhudzidwa. Zokambirana za akadaulo osiyanasiyana abungwe la FAO zinachitika m'magawo awiri, Gawo loyamba linachitika kuyambira pa 20 mpaka pa 24 Meyi 2013 pamene gawo lachiwiri linachitika kuyambira pa 3 mpaka pa 7 Febuluwale 2014 pamene akadaulo osiyanasiyana anaunikira mozama . Ndondomekozi zakonzedwa moganizira mfundo ndi maganizo akuya pam'mene zinthu zimakuyenerakukhalira monga; kufunika kwa kusasiyana mphamvu ndi kusasalana pakati pa anthu, kutenga nawo mbali ndi kuonetsetsa kuti palibe yemwe akutsalira, kutumikira modzipereka pantchito yoyenera kugwira, kutsatira malamulo ndi kulemeleza ma ufulu achibadwidwe pa dziko lonse lapansi. Ndondomekozi ndizogwirizana ndi ufulu wa anthu padziko lonse ndipo zimapititsa malamulo patsogolo. Ndondomekozi zikuthandizira malamulo abungwe la FAO pamagawo onse okhudzidwa. Ndondomekozi zapangidwa motsatira zina mwa ndondomeko za bungwe la FAO monga; Ndondomeko za Ulimi wa Nsomba Wodalirika No. 10 "Kuchulutsa Gawo Lotengedwa ndi Alimi a Nsomba Ang'onoang'ono mu Ntchito Zothetsa Umphawi ndi Zowonetsetsa kuti Anthu ali ndi

Chakudya Chokwanira", komanso ndondomeko zina zokhazikika ndi zodziwika bwino monga Ndondomeko Zothandiza Kayendetsedwe Kabwino ka Umwini wa Malo Ochitirako Usodzi, ndi nkhalango mokhudzana ndi ntchito yowonesetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira (Ndondomeko za Zaumwini), ndondomeko zosakakamiza zothandiza machitachita okwaniritsa motsogola ufulu wokhala ndi chakudya chokwanira (Ndondomeko za Ufulu wa chakudya), malinga ndi m'mene zikugwirizanirana ndi ndondomeko zino.Maiko ndi ena onse okhudzidwa akulimbikitsidwa kuti awerenge ndondomeko zinazi, komanso mfundo zosiyanasiyana za m'mayiko ndi m'zigawo kuti awunikemo zina ndi zina zothandiza kupititsa izi patsogolo.

Loyamba

Mawu Otsogolera

1. Zolinga

1.1 Cholinga cha ndondomekozi ndi:

a) Kupititsa patsogolo kutengapo gawo kwa ntchito zing'onozing'ono za usodzi poonesetsa kuti chakudya chokwanira chikupezeka pa dziko lapansi komanso kuthandizira kukwaniritsa ufulu okhala ndi chakudya chokwanira.

b) Kuthandizira chitukuko cha m'madera amene amatenga mbali mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi komanso kuthetsa umphawi ndi kukweza chuma cha asodzi ndi anthu ogwira ntchito zokhudza nsomba potsata njira zamakono zosamalira malo omwe wopezeka nsomba.

c) Kukwaniritsa kagwiritsidwe koyenera ndi kosamala poteteza zamoyo zam'madzi zodyedwa ndi anthu mogwirizana ndi mfundo zakagwiridwe kantchito ndi kuonesetsa kuti usodzi ukuchitika moyenera.

d) Kulimbikitsa ntchito zing'onozing'ono za usodzi po konza tsogolo labwino pa chuma, umoyo ndi kuteteza chilengedwe.

e) Kupereka upangiri ku maiko ndi magulu okhudzidwa pachitukuko ndi kulimbikitsa njira zotetezera zachilengedwe ndi malamulo popititsa patsogolo njira zoyenera kutsata ntchito zing'onozing'ono za usodzi.

f) Kufalitsa mauthenga odziwitsa anthu, kulimbikitsa maphunziro kudzera mu chikhalidwe, ntchito, kutengapo mbali komanso kuthekera kwa ntchito zingo'nozing'ono za usodzi ndi ulimi wa nsomba pogwiritsa ntchito nzeru zamakolo.

1.2 Zolinga zimenezi zikuyenera kukwaniritsidwa potsata njira zolimbikitsira ufulu wa anthu, pothandiza madera omwe muli anthu amene amagwira ntchito zing'onozing'ono za usodzi, pogwira ntchito ndi amayi ndi abambo popanga ziganizo ndi kutenga nawo gawo pa kagwiritsidwe kazipangizo zomwe zimafunikira mu usodzi. , Kuthandiza mayiko okwera kumene ndi zipangizo ndi upangiri kuti anthu osowa asaponderezedwe koma apindule nawo.

2. M'mene ndondomekozi zilili

2.1 Ndondomekozi nzosakakamiza ndipo zikukhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi padziko lonse ndi chidwi chapadela

pazofuna zamayiko okwera kumene.

2.2 Ndondomekozi ndizofunikira ku ntchito zing'onozing'ono za usodzi ku nyanja ndi kuntunda, kuti amayi ndi abambo azitenga nawo gawo kuti nsomba zizipezeka m'misika. Ndondomekozi zikuzindikira kuti pali kulumikizana pakati pantchito zing'onozing'ono za usodzi ndi ulimi wa zam'madzi koma ndondomekozi zatsamira kwambiri pa za usodzi.

2.3 Ndondomeko ndi zamamembala a bungwe la FAO komanso ena onse m'maiko, mabungwe padziko lonse, ndi onse ogwira ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Cholinga cha ndondomekozi nkuthandiza nthambi za kafukufuku ndi maphunziro apamwamba, mabungwe omwe siaboma ndi ena okhudzidwa kukonzanso kagwiritsidwe kabwino kachilengedwe cha m'madzi.

2.4 Ndondomekozi zikuzindikira kuti ntchito zing'onozing'ono zausodzi zosiyanasiyana zilibe kumasulira kovomerezeka motero sizikupereka tanthauzo koma mau oti 'ntchito zing'onozing'ono za usodzi' ndipo sakuneneratu m'mene ndondomekozi zingagwiritsidwire ntchito m'mayiko osiyanasiyana malinga ndi zosowa zawo. Ndondomekozi ndizofunikira kwa asodzi ang'onoang'ono ndi ena omwe amagwira ntchito za usodzi kuti adzingopeza chakudya cha tsiku ndi tsiku komanso asodzi atha kupeza mavuto osiyanasiyana mosavuta pakagwiridwe kantchito yao. Powonetsetsa kuti pali kagwiridwe kabwino ka ntchito ndiponso chilungamo, ndikofunika kudziwa tanthauzo la mau oti 'ntchito zing'onozing'ono za usodzi' ndikagwiridwe ntchito kake, komanso kudziwa magulu ofunika kupatsidwa chidwi chochuluka. Izi zikuyenera kuchitika m'magawo akuluakulu ndi ang'onoang'ono a m'dziko, kapena m'mayiko potengera nthawi zosiyanasiyana zomwe ndondomekozi zingagwiritsidwe ntchito. Akuyenera kuwonetsetsa kuti kuzindikira ndondomekozi ndi kagwiritsidwe ntchito kake katsatire njira zoyenera pololа magulu osiyanasiyana kutenga nawo mbali ndi cholinga choti maganizo a amayi komanso abambo adzimveka mosakondera gulu limodzi mwa awiriwa. Magulu onse okhudzidwa athandize ndi kutenga mbali m'madongosolo onse.

2.5 Ndondomekozi zitanthauziridwe ndi kugwiritsidwa ntchito mogwirizana ndi malamulo a dziko komanso nthambi zake.

3. Mfundo Zotsogolera

3.1 Ndondomeko izi zakonzedwa potsatira mfundo za padziko lonse za ufulu wa anthu, mfundo zapadera zokhudza usodzi komanso ntchito zina zachitukuko. Ndondomekozi zikutsatira mkumano wa Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko Onse pa Nkhani ya Chitukuko Chokhalitsa, wa Rio+20, omwe unatulutsa chikalata chotchedwa 'Tsogolo Lomwe Tikufuna'. Ndondomekozi zikulongosola malamulo a ntchito za usodzi ndi mfundo zina zofunikira popereka chidwi chapadera ku zinthu zokhudza

magulu omwe miyoyo yawo kawirikawiri imakhala pachiopsyezo ndi osowa thandizo ndi kufunika kokwaniritsa ufulu okhala ndi chakudya choyenera.

1. Kulemekeza ufulu wa chibadwidwe za munthu: Pozindikira kuti munthu aliyense ali ndi ufulu wachibadwidwe ofanana , nthambi zokhudzidwa zizindikire, kulemekeza, kulimbikitsa ndi kuteteza ma ufuluwa ndi m'mene amagwilira ntchito m'madera okhudzidwa. Pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi, ndondomeko za padziko lonse za ufulu wa anthu zimati: anthu azichita zinthu pamodzi mosamanana, mosagawanika, modalirana ndi kukhala mwa ubale, kupewa kusankhana mitundu, ndi kulimbikitsa umodzi, kutengapo mbali, kukhulupirika ndi kumvera malamulo. Mayiko alemekeze komanso kuteteza anthu omenyera ufulu wa anthu akalowelerapo pantchito zing'onozing'ono za usodzi. Otengapo mbali omwe siaboma kuphatikizapo ochita malonda okhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi ali ndi udindo olemekeza ufulu wa anthu. Mayiko ayang'anire zochitika mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi zomwe otengapo mbali osayimira boma angagwire ndi kuchuluka kwake pofuna kuwonetsetsa kuti akutsatira ndondomeko molemekeza ufulu wa anthu.

2. Kulemekeza zikhalidwe: Kuvomereza ndi kulemekeza kachitidwe kazinthu komwe kalipo kale, nzeru za makolo ndi zina zopezeka kudera zokhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi, kugwira ntchito ndi anthu a m'dera ndi magulu akuderako motsatira zikhulupiliro zamakolo komanso magulu a athu omwe amaponderezedwa kuchifukwa chakuchepa kwamtundu wawo kapena opanda mpamvu. Kulimbikitsa amayi kukhala m'maudindo komanso kuchita zinthu moganizira ndime 5 ya ndondomeko za Mfundo Zotheretseratu Kusalidwa kwa Mtundu Uliwonse.

3. Kusasalana: kulimbikitsa madera a asodzi ang'onoang'ono kupewa tsankho lokhazikitsidwa ndi ndondomeko zotsogolera kachitidwe ka zinthu ndi ndi tsankho pamene ntchito zikugwiridwa.

4. Kusasiyanitsa chiwerengero cha amuna ndi akazi ndi magawo omwe amatenga nawo pazochitika Ndikofunika kuzindikira kufunika kwa gawo la amayi mu usodzi, maufulu awo ndi kupereka mwayi ofanana pakatoi pa akazi ndi amuna ndipo izi ziyenera kulimbikitsidwa.

5. Kusasiyanitsa chiwerengero cha anthu a mitundu, magulu ndi magawo osiyanasiyana pazochitika: Kulimbikitsa chilungamo mosalabadira mitundu koma molemekeza malamulo zikueyenera kulimbikitsidwa. Kusiyana pakati pa amayi ndi abambo kuzindikiridwe ndipo ndondomeko zolimbikitsa kusasiyanaku zitsatidwe pogwiritsa mfundo zapadera zothandiza kuti pasakhale kusiyana pakasi pa anthu,

makamaka pofuna kuteteza magulu omwe moyo wawo umakhala pachiopyezo nthawi zambiri komanso kuponderezedwa.

6. Anthu apatsidwe mwayi opereke maganizo awo ndi kutenga mbali muzochitika: Kuonetsetsa kuti anthu akutengapo gawo mwaufulu pa zochitika zonse. Izi zikutsatira ndondomeko za Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko pa Dziko Lonse Zokhudza Ufulu wa Chibadwidwe wa Anthu Omwe Amakhala M'malo awo Achibadwidwe, popanga ziganizo zokhudza usodzi ndi madera omwe asodzi ang'onoang'ono amagwilira ntchito, malo oyandikana nawo, ndi kuonetsetsa kuti kusiyana mphamvu pakati pa okhudzidwa sikuli kosiyana. Izi kuphatikiza kumva maganizo a anthu omwe angakhudzidwe ndi ziganizo zopangidwazo ndi zina zochitika ziganizozi zisanakhalepo komanso zisanayambe kugwira ntchito ndi kupereka mayankho oyenera okhudza maganizo awo.

7. Kutsatira malamulo: Kutsata malamulo pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi pogwiritsa ntchito malamulo opezeka m'zilankhulo zomwe zimagwiritsidwa ntchito m'deralo komanso zomveka kwa onse. Malamulowa akhale opanda tsankho ndipo agwirizane ndi mfundo zina za m'dziko ndi dziko lonse. Izi zichitike pozindikira kuti ntchito zina m'zigawo ndi m'mayiko zikugwiridwa mongodzipereka zomwe motsatira mfundo zoyikidwa.

8. Kuchita zinthu poyera: Kufotokoza ndi kulengeza bwino mfundo, malamulo ndi ndondomeko mu zilankhulo zonse zogwiritsidwa ntchito, kulengeza ziganizo zonse zochitika muzilankhulo zogwiritsidwa ntchito ndi zofikirika ndi onse

9. Kachitidwe ka zinthu kolemekeza malamulo: Adindo, nthambi za boma komanso magulu onse okhudzidwa oyima paokha agwire ntchito yawo motsatira malamulo.

10. Ntchito za chuma, zinthu zothandiza miyoyo ya anthu yatsiku ndi tsiku, ndi zachilengedwe zosathera panjira: Kugwiritsa ntchito njira zoyenera zopewera komanso kuthanirana ndi chiopsyezo chomwe zotsatira zake nzosafunika monga; kagwiritsidwe ntchito kopyola muyeso ka zachilengedwe zokhudza usodzi ndi machitachita obweretsa mavuto pa zachilengwedwe, moyo wa anthu watsiku nditsiku komanso pa chuma.

11. Kugwiritsa ntchito njira zoyang'ana mbali zonse za zinthu zogwirizana: Kuzindikira njira zogwilira ntchito zing'onozing'ono za usodzi zomwe zimadalira kumvetsa m'mene chilengedwe chopezeka pamalo chimagwilira ntchito modalirana ngati njira imodzi yothandiza kuteteza , zinthu zonse zokhudza madera omwe kuli ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Kuonetsetsa kuti pali kulumikizana ndi kudalirana pakati pa ntchitozi ndi magawo ena a amoyo wa anthu.

12. Udindo wa anthu pazochitika: Kulimbikitsa m'gwirizano pakati pa anthu ndi magulu okhudzidwa pa ntchito yosamalira chilengedwe

13. Kuthekera kosavuta ndi kokwanira pobweretsa chuma ku anthu: Kuonetsetsa kuti pakukonzedwa mfundo ndi ndondomeko zokomera ntchito zing'ong'onozing'ono za usodzi popititsa patsogolo chuma, makhalidwe a anthu. Mfundo zikhale zogwirizana ndi momwe zinthu ziliri komanso zothekera komanso mopitilira ngakhale mu nthawi yovuta.

4. Kulumikizana pakati pa ndondomekozi ndi mfundo zam'mayiko osiyanasiyana

4.1 Ndondomekozi zimasulilidwe ndi kugwiritsidwa ntchito mogwirizana ndi malamulo a dziko komanso mozindikira ntchito zina nzongodzipereka m'ndondomeko zokhazikika za m'zigawo komanso dziko lonse. Ndondomekozi zithandizire ntchito yomwe ikugwiridwa m'mayiko ndi m'mzigawo za dziko lapansi pofuna kulimbikitsa maufulu a anthu, kachitidwe koyenera kausodzi komanso kulimbikitsa chitukuko chokhazikika. Ndondomekozi zinakhazikitsidwa poonjezera ndondomeko zomwe zilipo kale zolimbikitsa usodzi oyenera ndi kugwiritsa bwino ntchito mfundo zolembedwa mwatsatanetsane.

4.2 Ndondomekozi zisachepetse kapena kuletsa ena mwa maufulu ndi ma udindo omwe dziko likuyenera kutsatira malingana ndi malamulo a padziko lonse. Ndondomeko zotsogolerazi zikhonza kugwiritsidwa ntchito yongokozanso kapena kubweretsa malamulo ena atsopano owonjezera pakayendetsedwe ka ntchito zing'onozing'ono za usodzi.

Gawo Lachiwiri Ntchito
za usodzi Zogwiridwa moyenera

5. Kayendetsedwe ka umwini wa malo ndi zinthu zina mu ntchito zing'onozong'ono za usodzi ndi kagwiritsidwe ntchito koyenera ka zinthu.

5.1 Ndondomekozi zikuonetsa kufunika kogwiritsa ntchito moyenera zachilengedwe zosiyanasiyana zam'madzi pokwaniritsa zosoweka za m'badwo uno ndi yamtsogolomu pachitukuko komanso chilengedwe. Amene amatenga mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi akuyenera kuteteza ufulu okhala ndi umwini wazinthu, chikhalidwe chawo ndi m'mene amapezera zosowa zamoyo wawo. Akuyenera kutenga nawo mbali pantchito zachitukuko zokhalitsa. Ndondomekozi zikulimbikitsa kagawidwe kofanana ka phindu lochokera mu zinthu zomwe zimapezeka pakayendetsedwe koyenera kantchito zausodzi ndi kasamalidwe kazachilengedwe zosiyanasiyana polora asodzi ang'onoang'ono ndi ogwira ntchito amuna ndi a akazi kupindula nawo.

5a Kayendetsedwe koyenera ka umwini wa malo

5.2 Magulu onse okhudzidwa akuyenera kudziwa zakayendetsa koyenera ka umwini wamalo, mitsinje ndi nyanja komanso nkhalango zimene zili zinthu zokhudza ntchito zing'onozing'no za usodzi. Kusamalira kwa magawowa achilengedwe kuli ndi kuthekera kothandiza kukwaniritsa ma ufulu a anthu, kupeza chakudya chokwanira, kuchepetsa umphawi, kukhala ndi njira zodalirika zopezera zofunika pamoyo watsiku ndi tsiku. Kwakukulu kwake izi zitha kuthandiza pakukwera kwaa chuma ndi chitukuko m'madera am'midzi komanso kwa anthu onse .

5.3 Maiko mogwirizana ndi malamulo awo, awonetsetse kuti asodzi ang'onoang'ono, anthu ogwira ntchito za usodzi ndi onse m'madera oterewa sakupondelezedwa ku maufulu awo, komanso akuchita zinthu mogwirizana ndi kakhalidwe kawina ndi mzake, kulemekeza chikhalidwe pantchito yopha nsomba (za m'madzi ndi za pamtunda) Izi zichitike mopatsa chidwi chapadera kwa azimayi komanso molemekeza ufulu wa anthu wokhala ndi umwini wamalo ndi zinthu zina.

5.4 Maiko potengera malamulo awo, ndi onse amagulu okhudzidwa avomereze kulemekeza komanso kuteteza ufulu wa onse wokhudza umwini wa malo, ndipo izi zizichitika moganizira ufulu wa anthu akumadera omwe kumachitika ntchito za usodzi. Ma usodzi ang'onoang'gonowa ali kale ndi maufulu okhazikika potsatira miyambo yamakolo pazachilengedwe zam'madzi, malo ndi madera ochitirako usodzi. Poteteza ufulu okhudza umwini wa malo, mpofunika malamulo pankhaniyi atakhazikitsidwa ngati nkoyenera kutero. Maiko

akuyenerakutsata njira zovomerezeka pochita kaundula wa anthu amene ali ndi malo ndi kulemekeza zotsatira zake. Kachitidwe ka zinthu kokhazikika m'chikhalidwe cha anthu kumadera komwe anthuwo amawatenga kuti kakuyimira m'mene zinthu zimakuyenerakukhalira komanso zochitika zokhazikika pamiyambo yamakolo pakagwiritsidwe ntchito kazinthu zopezeka m'madzi, maufulu awo achibadwidwe komanso kumene mitundu ya anthu ndiyochepa akuyenera kusalalidwa koma kukhala nazo pazochitika m'mdera lawo. Izi zikulemekeza malamulo a ufulu wa chibadwidwe wa anthu padziko lonse.

Mfundo za Bungwe la Mgwirizano wa Mayiko pa Dziko Lonse Zokhudza Ufulu wa Chibadwidwe wa Anthu Omwe Amakhala M'malo awo Achibadwidwe (UN DRIP) ndi za malamulo apa dziko lonse okhudza ufulu wa magulu a anthu omwe achiwerengero chochepa poyerekeza ndi mitundu ina, pachipembedzo chawo ngakhalenso chiyankhulo akuyenera kuganiziridwa mwapadera. Pamene kusintha kwa malamulo aakulu ndi aang'ono adziko kukulimbikitsa ma ufulu a amayi motsutsana ndi miyambo yakudera, onse okhudzidwa akuyenera kugwilira ntchito limodzi kuti kusintha kumeneku kuchitike mwa malamulo amiyambo yamakolo okhudza umwini wamalo ndi zinthu zina zofanana nazo.

5.5 Maiko azindikire kufunika kwa magawo wotenga anthu akumadera omwe kumagwiridwa ntchito zing'onozing'ono za usodzi, anthu omwe amakhala kumalo omwe ndi kwawo pantchito zosamalira chilengedwe poyeziyendetsera limodzi.

5.6 Pamene maiko ali ndi ulamuliro pazachilengedwe zam'madzi (kuphatikiza usodzi ndi ntchito zina zokhudza nsomba) akuyenera kukhazikitsa mfundo pa kagwiritsidwe ka zinthuzi ndi maufulu a umwini wamalo ndi zina zofanana nazo komanso, chikhalidwe cha anthu akuderalo, kapezedwe kachuma komanso za chilengedwe.

5.7 Malinga ndi mfundo 6.18 ya Malamulo Owonesetsera kuti Ntchito za Usodzi Zikugwiritsa Ntchito Njira Zabwino, maiko akuyenerakupereka chilorezo kwa amene amatenga nawo mbali mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi omwe ali pansi pa ulamuliro wawo. Izi zidzathandiza poonetsetsa kuti magulu maka a anthu omwe moyo wawo umakhala kuti ndi oponderezedwa uzitenga nawo mbali mofana ndi ena. Mwa zina, pakhazikitsidwe malo apadera ogwirirako ntchito zing'onozing'ono za usodzi Ntchito zing'onozing'ono za usodzi ziyenera kuganiziridwa m'migwirizano yokhudza malo ochitirako usodzi isanakhazikitsidwe pakati pa mayiko omwe akukwera kumene ndi magulu obwera kuchokera kwina.

5.8 Maiko akuyenera kukhazikitsa njira zolimbikitsira kuti asodzi ang'onong'ono azikhala ndi mpata ofanana ndi magulu ena pogwiritsa ntchito zinthu zofunika pa usodzi, monga kugawanso zinthu zofunikira pantchitoyi motsata ndondomeko.

5.9 Maiko akuyenera kuonetsetsa kuti anthu amene amatenga mbali pantchito zing'onozing'ono zausodzi sakuthamangitsidwa kumalo popanda chifukwa komanso ufulu wawo wa malo sukuthetsedwa kapena kuponderezedwa. Maiko azindikire

kuti m'madera omwe m'machitika ntchito zing'onozing'ono za usodzi mulibe kukokerana kwa malo pakati pa asodzi wobwera ndi magulu ena zimene zingapyinje ma ufulu asodzi ang'onoang'ono. Zindikirani kuti anthu osatetezedwa ndi osalidwa ndi amene amavutika kwambiri ndi mpikisanowu. Magulu ofookawa akhonza kufunika chithandizo chapaderadera makamaka pamene miyoyo yawo yaphinjika ndi zinthu zina za chitukuko cha magulu enawo.

5.10 Maiko komanso magulu okhudzidwa, asanapange zitukuko zikuluzikulu zomwe zikhonza kukhudza miyoyo ya anthu amene amatenga mbali m'ntchito zing'onozing'ono zausodzi. Akuyenera kugwiritsa ntchito kafukufuku kuti aganizire zotsatira za ntchito za chitukuko zimene akufuna pakakhalidwe ka anthu, ntchito zawo zachuma ndi zachilengedwe. Akuyenera kumva maganizo alimi molingana ndi m'mene malamulo a dziko akunenera.

5.11 Maiko, kudzera kumabungwe amalamulo komanso kayendetsedwe kazinthu akuyenerakutsatira njira zosavuta zothandizira kuthana ndi mavuto aumwini wamalo monga m'mene malamulo adziko akunenera kwa amene amatenga nawo mbali mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi kuphatikizapo magulu omwe miyoyo yawo ndiyosatetezedwa kweni kweni. Maiko ayenera kupereka njira zothetseratu mavuto akachitika. Njirazi ziyenera kukwaniritsidwa mwamsanga mogwirizana ndi malamulo a dziko ndipo zina mwa izo ndi kubwezeretsa kwa eni ake zinthu zimene zinatengedwa popanda chilorezo, kulipira ndalama kwa munthu amene waonongeredwa kapena kulandidwa katundu wale monga malo ngati chipukuta misonzi.

5.12 Maiko akuyenerakuchilimika pa ntchito yoonesetsa kuti asodzi ang'onoang'ono amene madela awo anakhudzidwa ndi mavuto angozi zachilengedwe kapena nkhondo apatsidwanso ufulu ogwiritsa ntchito malo achikhalidwe chawo pa ntchito za usodzi ndi malo a m'mbali mwa nyanja. Zinthu zimenezi zichitike moganizira kufunika koteteza zamoyo za m'madzi zomwe zimapezetsa anthu chakudya kapena ndalama. Maiko akuyenera kukhazikitsa njira zothandizira anthu m'madera amene amatenga mbali pa usodzi omwe anaphwanyiridwa ufulu wawo kuti ayambirenso kukonza miyoyo yawo ndi zinthu zomwe amachita pofuna pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Njira zimenezi zitsagane ndi kuthetsa tsankho lomwe amayi amachitiridwa pa umwini wa malo maka pamachitika ngozi zachilengedwe kapena nkhondo.

5b. Kusamala zinthu zamoyo za m'madzi moyenera

5.13 Maiko ndi onse oyendetsa ntchito za usodzi akuyenera kugwiritsa ntchito njira zokhazikika zosamalira ndi kugwiritsira moyenera chilengedwe cham'madzi. Izi zithandiza kuti pogwiritsa bwino ntchito chilengedwe chomwe chimadalirana motero pakhale kupezeka kwa chakudya chokwanira. Alimbikitsenso kayendetsedwe kabwino koyenera kazinthu malingana ndi malamulo a dziko ndi amaiko ndi mgwirizano yokhudza kutenga mbali mosakakamizidwa ndi Phindu

lokhudza amene amatenga mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi.

5.14 Magulu onse akuyenera kuzindikira kuti ufulu ndi udindo zimagwira ntchito mogwirizana. Ufulu wa umwini malo umayenda bwino ngati akuwugwiritsa ntchito mogwirizana ndi udindo wake. Anthu amene amatenga mbali mu ntchito zing'onozing'ono zausodzi akuyenerakugwiritsa ntchito njira zoyenera zomwe zimachepetsa chiopsezo ku chilengedwe cham'madzi kuphatikizapo zamoyo zosiyanasiyana zokhudzana ndi chilengedwecho komanso kuwonetsetsa kuti akuteteza malo ochitirako usodzi.

5.15 Maiko akuyenera kutenga mbali pokwaniritsa zinthu, kupereka ukadaulo ndi kuthandiza anthu amene amatenga nawo mbali m'ntchito zing'onozing'ono za usodzi kuti azitenga udindo oyendetsa ntchito zokhudza kasamaliridwe ka nsomba zimene amadalira pa moyo wawo tsiku ndi tsiku. Izi zichitike moganizira malamulo ndi ufulu okhudza kukhala ndi malo wovomerezeka.

Maiko akuyenera kupereka mpata wofanana kwa amene amatenga mbali pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi - makamaka amayi ndi magulu a anthu amene amakhala pachiopsyezo m'zambiri. Mpatawu upereke danga lokonnso zoyerekeza kakwaniritsidwe kachilinganizochi, kuphatikiza kayendetsedwe kamalo kumene kumapezeka zinthu zothandiza pamoyo watsiku nditsiku. Njira zoyendetsera zinthu zothandizira magulu osiyanasiyana kuyendetsa nawo ntchito limodzi ziyenera kulimbikitsidwa mogwirizana ndi mamulo a dziko.

5.16 Maiko akuyenerakuonetsesa kuti pali njira zowongolera, zoyang'anira ndi kuwonesetsa kuti palibe chisawawa polimbikitsa kugwiritsa ntchito njira zomwe zilipo kale kudera zomwe ziri zoyenera kwa anthu amene amatenga mbali mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Maiko akuyenera kupereka thandizo kuzochitika zadongosolo lokhazikika lokhudza asodzi ang'ono ang'ono otenga nawo mbali pantchito zoksamalira nsomba. Boma lilimbikitse kasamalira kwa zokolora zamagulu a anthu osiyanasiyana amene amatenga nawo mbali pa ntchito zosamalira chilengedwe. Maiko awonetsetse kuti pali njira zoyenera zokwaniritsira ndondomeko zimene ndi kuonesetsa kuti pali njira zothetseratu usodzi owononga chilengedwe komanso osavomerezedwa ndi lamulo. Maiko ayesetse kulemba mukawundula ntchito zonse za usodzi. Asodzi ang'onoang'ono akuyenera kuthandizira kuwonetsetsa kuti ntchito zonse zikugwiridwa mwadongosolo.

5.17 Maiko akuyenera kuonetsetsa kuti udindo okhudza kayendetsedwe kantchito zokhudza nsomba mokhazikika kakupereka mpata olora magulu osiyanasiyana kutenga nawo mbali pofotokozera anthu momveka bwino komanso motsata malamulo. Magulu onse ali ndi udindo oyendetsa ntchito monga momwe anagwirizanirana. Zonse zoyenera kuchita powonetsetsa kuti amene amatenga nawo mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi akutenga nawo gawo pakayendetsedwe ka mabugwe a m'dziko momwemo komanso akunja paukadaulo uteteza nsomba. Mpofunika kuonetsetsa kuti anthu akutenga nawo gawo muzochitika zomwe mabungwewa

amagwiritsa ntchito popanga ziganizo ndi ndondomeko zogwilira ntchito zoteteza nsomba.

5.18 Maiko komanso anthu amene amatenga mbali muntchito zing'onozing'ono zausodzi akuyenera kulimbikitsa ndi kuthandiza magawo a amayi ndi abambo pakakonzedwe ndi , kanyamulidwe ndi malonda ake. Magulu onse awonetse chidwi polimbikitsa amayi kutenga nawo mbali pantchitozi ndipo pakhazikitsidwe njira zapadera zokwaniritsira izi.

5.19 Pamene pali zopinga zokhudza madzi ndi madera opezeka nsomba amene ali m'malire amayiko, maiko akuyenera kugwira ntchito limodzi poteteza umwini wamalo omwe anthu akumadera omwe kumachitika ntchito za usodzi zing'onozing'ono.

5.20 Maiko akuyenera kupewa ndondomeko ndi njira zokhudza chuma zomwe zingabweretse kusodza kopitilira muyezo komwe kuli ndi kuthekera kosokoneza miyoiyo ya anthu maka pa ntchito zazing'onozing'ono zausodzi.

6. Chitukuko, kapezekedwe kantchito ndi magwiridwe antchito abwino.

6.1 Magulu onse aganizire njira zabwino zogwirira ntchito zing'onozingo'no za usodzi zimene zili zodalira chilengedwe cha nsomba komanso njira yomwe imalimbikitsa kupezeka kwa zinthu zothandizira moyo wa anthu tsiku ndi tsiku. Pakhale chidwi chokwanira potukula chikhalidwe cha anthu ndi chuma powonetsetsa kuti alimi akupatsidwa mphamvu komanso akutha kugwiritsa ntchito zawo mwaufulu.

6.2 Maiko akuyenera kulimbikitsa ntchito zopindulira dziko pakapezedwe ka ndalama powonetsetsa kuti pali anthu ophunzitsidwa bwino m'magawo a ntchito zawo monga zaumoyo, maphunziro, kuwerenga ndi kulemba, luso losiyanasiyana pakagwiritsidwe ntchito makina amakono monga intaneti ndi luso lina lofunika nzeru zozama zimene zili ndi kuthekera kokweza ntchito zoteteza chilengedwe cha m'madzi. Maiko achite zoyenera powonetsetsa kuti anthu akumadera komwe kumagwiridwa ntchito za usodzi zing'onozing'ono ali ndi mwayi opindula nawo kudzera m'ntchito zosiyanasiyana zokhudza dziko kapena madera ena adzikolo. Zinthuzi ndi monga kulimbikitsa ukhondo, madzi akumwa abwino komanso njira zopangira mphamvu zoyisanasiyana. Kulolera amayi, anthu okhala m'malo awo achibadwidwe, magulu omwe amakhala pachiopsezo pazinthu zosiyanasiyana komanso oponderezedwa akuyenera kupatsidwa mpata ogwiritsa nawo ntchito zinthu zowapezetsa zofunika pamoyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Maufulu awo akuyenera kuvomerezedwa ndi kulimbikitsidwa ngati njira imodzi yothetsa tsankho pakati pa anthu.

6.3 Maiko akuyenera kupereka chitetezo pamene anthu akutenga nawo mbali pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Akuyeneranso nkuganizira zinthu zomwe ziri zapadera m'madera amene mumagwiridwira ntchito zing'onozing'ono za usodzi ndi kupereka chitetezo pa ntchito yokonza ndi kugulitsa nsomba.

6.4 Maiko akuyenera kuthandiza kutukula anthu wokhala m'madera omwe kumagwiridwa ntchito zing'onoang'ono za usodzi pantchito zakasungidwe ndi kubwereketsana ndalama, kulimbikitsa chitetezo chawo kumavuto ogwa mwadzidzidzi Awonetsetsenso kuti amayi ali ndi mwayi ofikiridwa ndi zinthu ngati zimenezi .

6.5 Maiko akuyenera kudziwa zinthu zimene amachita amuna ndi akazi pa ntchito za usodzi ung'onoung'ono zimabweretsa chuma chotani komanso ntchito zake zimafuna luso lotani zomwe mwina anthu akunja kwa ntchitozi sangazidziwe kapena kuzimvetsa bwino.

Zochitika zonse ziyenera kuganiziridwa, moteteza nsomba uku anthu akuchita ntchito zina mwa apa ndi apo, kapena mongozithandizira kupeza zosowa zatsiku nditsiku. Mwayi wamaphunziro antchito zokhudza nsomba zikuyenera kulimbikitsidwa makamaka pakati pa amayi ndi magulu ogwira ntchito zokhudza nsomba zikagwidwa omwe miyoyo yawo imene kawirikawiri imakhala pachiwopsezo

6.6 Maiko akuyenera kulimbikitsa kagwiridwe kantchito kabwino pakati pa anthu amene analembedwa ntchito zazing'onzing'ono za usodzi. Izi zitha kukhala ntchito zimene zinalembetsedwa m'kawundula waboma komanso zina zosalembetsedwa. Maiko akuyenera kukhazikitsa njira zowonetsetsa kuti ntchito za usodzi zolembetsedwa m'kawundula waboma komanso ayi zikuganiziridwa popititsa ntchito za usodzi zing'onozing'ono molingana ndi malamulo adziko.

6.7 Maiko akuyenera kupeza njira zoonetsetsa kuti ntchito za usodzi zing'onozing'ono komanso anthu ogwira ntchito za usodzi zikhale mogwirizana ndi ufulu wa anthu okhala ndi moyo wabwino mogwirizana ndi maufulu ovomerezeka ndi dziko komanso mfundo zamaiko onse. Maiko akuyenera kupereka zipangizo zothandizira anthu m'madera kumene kumachitikira usodzi ung'onoung'ono kuti azichita zitukuko zokhazikika. Maiko akuyenera kukhazikitsa ntchito ndi ndondomeko zokomera anthu onse monga zachuma, kakoloredwe kopindulira wina aliyense ka zachilengedwe za m'nyanja ,malo akumtunda ndi n'cholinga choti anthu amene amatengapo mbali pantchito zing'onozing'ono zausodzi maka amayi akupeza nawo cholowa molingana ndi luso limene awonetsa pantchitoyo komanso chuma chopezeka pantchitoyo. Maiko akuyenera kulimbikitsakusamalira zachilengedwe kuti zikathe kupezeka mwa nthawi yaitali.

6.8 Maiko ndi magulu ena okhudzidwa akuyenera kulimbikitsa njira zobweretsa chuma zimene zilipo kale m'maderamu ndikulimbikitsanso asodzi ang'onoang'ono kupeza njira zina zopezera ndalama posamangodalira usodzi okha. Pofunikanso kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito kabwino kazinthu zachilengedwe kuti zipitilire kupezekabe komanso asamangodalira njira imodzi akafuna yopezera zinthu zowathandiza pamoyo wawo watsiku ndi tsiku. Ntchito za asodzi ung'onoung'ono ziyenera kudziwika bwino pa m'mene ikuthandizira pakabweretsedwe kachuma m'dziko

komanso ndi njira zimene zikutsatidwa kuti zipitilire kubweretsa phindu moyenera. Anthu amene amatenga nawo mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi akuyenera kupindula mofanana kuchokera ku ncthito zina zamdera lawo monga zokopa alendo komanso ulimi oweta nsomba. wa za m'madzi.

6.9 Magulu onse okhudzidwa akuyenera kutenga nawo gawo pomanga mfundo zoyenera zofikira asodzi ang'onoang'ono maka amuna ndi akazi kuti adzigwira ntchito zawo m'malo otetezedwa opanda umbanda, ziwawa, kuba erana, kuchitirana nkhanza zochitirana pogonana, ziphuphu komanso kugwiritsa ntchito mphamvu za udindo mosayenera. Magulu onse aonetsetse kuti payikidwa pali njira zothana ndi m'chitidwe ochitira nkhanza amayi akamagwira ntchito za usodzi zing'onozing'onozi. Maiko awonetsetse kuti anthu amene ochitiridwa nkhanza monga kuzunzidwa m'mmakomo kapena kudera akathe kupeza chilungamo.

6.10 Maiko komanso anthu amene amatenga mbali mu ntchito zing'onozing'ono za usodzi kuphatikizapo atsogoleri osankhidwa am'madera potsatira miyambo yawo akuyenera kumvetsetsa ndi kulemekeza asodzi obwera kuchokera ku madera ena, kuvomereza kufunika kwa athu ochokera kwinawa pa ntchito zingo'nozing'ono za usodzi pozindikira kuti asodzi amayendayenda kwambiri posaka kumene kuli nsomba.

Maiko ndi ena onse otengapo mbali pantchito zing'onozing'ono zokhudza usodzi akuyenera kugwilira ntchito limodzi poonetsetsa kuti pakhazikitsidwa njira zoyenera zovomereza ogwira ntchito za usodzi amene amatsatira kumene kuli nsomba kuti azitha kutsatira ulamuliro wakudera kumene apitako malingana ndi malamulo a dziko. Maiko akuyenera kuzindikira kufunika kogwira ntchito limodzi poyang'anira asodzi ndi ogwira ntchito zokhudza nsomba zing'onozing'ono pakati pamayiko. Ndondomeko zakayendetsedwe kazinthu zikuyenera kukonzedwa ndi magulu a anthu amene amatenga nawo mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi koma atayamba afunsidwa maganizo awo.

6.11 Maiko akuyenera kuzindikira ndi kuthana ndi zotsatira pa mayendedwe asodzi omwe amadutsa malire amayiko zimene zingathandize kubweretsa kusamvetsetsana pakachitidwe ka zinthu pa usodzi waung'onoung'ono. .

6.12 Maiko akuyenera kulimbikitsa kapezedwe ka chithandizo cha chipatala kwa anthu amene amakhala ndi kumagwilira ntchito yawo m'madera a usodzi waun'gonoun'gono. amMaiko akuyenera kuonetsetsa kuti paikidwa malamulo molingana ndi malamulo a dziko komanso ufulu wa anthu molingana ndi pangano la Pakati pa Mayiko pa Nkhani za Ufulu Wokhudza Chuma, Kakhalidwe ka Anthu ndi Chikhalidwe (ICESCR) ndi Bungwe Lowona za Ntchito pa Dziko Lonse (ILO). Magulu onse awonetsetse kuti umoyo ndi chitetezo cha anthu kumalo antchito kukhala mbali imodzi

ya kayendetsedwe kaulimi wasomba.

6.13 Maiko athetseratu m'chitidwe ogwiritsa anthu ntchito mokakamiza, kuika amayi, abambo ndi ana ngati chikole cha ngongole. Pakhale njira zoyenera zoteteza asodzi,ogwira ntchito, kuphatikiza anthu ongobwera kuchokera kwina.

6.14 Maiko awonetsetse kuti sukulu ndi ntchito zina zamaphunziro zikupezeka m'madera omwe amene kukuchitikira ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Izi zingathandize achinyamata kumapeza ntchito molingana ndi masophenya awo. Sukuluzi ziyenera kupereka mwayi wofanana kwa anyamata ndi atsikana komanso amayi ndi azibambo .

6.15 Anthu otenga gawo m'ntchito za usodzi zing'ongozing'ono akuyenera kuzindikira ubwino woti ana akhale ndi moyo wabwino komanso alandire maphunziro kuti tsogolo lawo komanso ladera likhale labwino. Ana kumapita ku sukulu, kutetezedwa ku nkhanza komanso ma ufulu awo akulemekezedwa.

6.16 Magulu onse agwirizane ndi kuvomereza ntchito za chitetezo cha asodzi kunyanja komanso kumtunda. Maiko akuyenera kukonza, kukhazikitsa, ndi kukwaniritsa malamulo ogwirizana ndi ndondomeko za bungwe la FAO, Bungwe lowona za ntchito la (ILO) ndi bungwe loona zamayenedwe apa nyanja la (IMO) okhudza kagwiridwe ka ntchito ndi chitetezo kwa asodzi ang'onoang'ono [3].

6.17 Maiko azindikirenso kuti chitetezo panyanja chimalumikizana ndi chitetezo cha anthu kumalo ogwilira ntchito kwa amene amatengapo mbali pantchito zausodzi ung'onoung'ono.. Chitetezochi chitha kukwaniritsidwa po gwiritsa ntchito malamulo adziko mogwirizana ndi asodzi eni ake, komanso mayiko ena ngati n'koyenera kutero. Chitetezo cha asodzi ang'onoang'ono chikhale m'ndondomeko zoyendetsera ntchito za usodzi. Maiko mwazina akuyenera kuthandiza kukonzanso njira zofalitsira mauthenga ochenjezera ngozi zochitika m' dziko, kuphunzitsa asodzi zachitetezo pa nyanja komanso malamulo okhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Mabungwe komanso adindo akuyenera kutenga nawo mbali polimbikitsa kafukufuku ndi maphunziro ozindikiritsa anthu m'mene angadzipulumutsire pa ngozi zapanyanja. , Maiko akuyenera kulimbikitsa kapezedwe kosavuta kamauthenga othandiza kulumikizana kwa asodzi ndi anthu amene angawafikire ndi thandizo lowapulumutsira mosavuta pamene akumana ndi ngozi za panyanja.

6.18 Potengera ndondomeko zozipereka pa ulamuliro wabwino olemekeza umwini wa malo, malo aza usodzi ndi nkhalango malingana ndi gawo 25[4] la malamulo. Magulu akuyenera kuteteza ma ufulu a anthu amene akutengapo mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi. Anthu okhudzidwa ndi nkhondo, akuyenera kuthandizidwa kuti asakhale moyo ovutika poloredwa kumagwiritsa ntchito njira zomwe anazizolowera kwao pakapezedwe kazinthu zosoweka pamoyo wawo wa tsiku ndi tsiku.

7. Kukonza nsomba zisanapite ku malonda

7.1 Magulu onse akuyenera kuzindikira ntchito imene asodzi ang'ono ndi ena

onse amagwira nsomba zikangophedwa. Magulu ogwira ntchito za usodzi akuyenera kumapanga ziganizo mwachangu pozindikira kuti pali zinthu zina zambiri zimene sizimayenda bwino zimene zimakhudza maka anthu amene kawirikawiri amapereweredwa ndi kusalidwa.

7.2 Magulu azindikire ntchito yomwe amayi amagwira pamene nsomba zangophedwa kumene ndipo pakhale njira zina zoonjezera m'mene gawo la amayi lingalimbikitsidwire pa ntchitozi. Maiko awonetsetse kuti amayi akukhala ndi ziwiya zogwilira ntchito zabwino panthawi yokonza nsomba zisanapite ku msika.

7.3 Maiko alimbikitse e ndi kupititsa patsogolo ntchito zachuma,zomangamanga, kagwiridwe kabwino kamabungwe ndi kuperekera maphunziro aluso losiyanasiyana kuti zikathandize pakagwiridwe ka ntchito pakati pa asodzi ang'onoang'ono . Izi zithandizenso kuwonetsetsa kuti nsomba zikukonzedwa mwapamwamba kuti zikathe kukopa mitengo yokwera ku misika..

7.4 Maiko ndi magulu ogwira ntchito zachitukuko awonetsetse kuti akudziwa zamalo amene kukupezeka anthu ogwira ntchito za usodzi zing'onozing'ono. Ayenera kulimbikitsa m'mene ntchito zimagwiridwira kuyambira pamene nsomba zangophedwa kumene kufikira pamene zikukagulitsidwa kumsika. Ngati izi zingachitike mwadongosolo zidzathandiza kukweza chuma ndi miyoyo ya anthu. Asodzi ang'onoang'ono akuyenera kulimbikitsidwa kukhazikitsa magulu pakagwiridwe kantchito zamalonda monga kugulitsa mipikisana mitengo, kakonzedwe ka nsomba ndi zina.

7.5 Magulu alimbikitse kupanga phindu pochepetsa kuwonongeka kwa nsomba pogwiritsa ntchito njira zabwino zamakono zokonzera nsomba. Kachitidwe kazinthu kagwirizane ndi kusintha kwa nyengo komanso kulimbikitsa ukhondo maka panthawi yokonza nsomba.

7.6 Maiko awonetsetse kuti misika ya m'dziko mwao komaso kunja pa malonda ansomba ikupezeka. Maiko awonetsetsenso kuti palibe kusalana ndi kuponderezana kwina kulikonse pamalonda ansomba. Maiko agwire ntchito pamodzi pokhazikitsa malamulo ndi njira zolimbikitsira malonda ansomba maka zochokera kwa asodzi ang'onoang'ono pakati pamayiko awo molemekeza maufulu a anthu ndi mfundo za wa Bungwe la lamalonda pa dziko lonse la World Trade Organisation.

7.7 Maiko alingalire mozama kufunika kwa malonda ansomba ndi zina zopangidwa kuchokera kunsomba pakati pa maiko awo. . Maiko aonetsetsenso kuti pamene akulimbikitsa malonda ansomba kumisika yakunja, izi zisaphwanye ndondomeko za adyedwe kabwino ka anthu amene amadalira nsomba ngati chakudya chofunikira nthupi

3. Izi zikukhudza mfundo zokhazikitsidwa m'mchaka cha 1968 zokhudza chitetezo cha asodzi ndi maboto ophera nsomba. (zimenezi panopa zinalembedwanso), Ndondomeko za bungwe lowona za chakudya ndi ulimi pa dziko lonse, Bungwe lowona za ntchito pa dziko lonse, Bungwe lowona mayenededwe apa nyanja padziko lonse za m'chaka cha 1980. Kupanga maboti ophera nsomba ndi zida zina za usodzi zokhazikitsidwa m' chaka cha 2010. Gawo 25 limakamba zakusemphana maganizo paumwini wa malo, malo ochitirako usodzi ndi nkhalango.

mwawo, kapena amene amadalira nsomba pa umoyo wawo. .

7.8 Maiko otenga nawo mbali pantchito zing'onozing'ono za usodzi ndi anthu ena okhudzidwa azindikire kuti phindu lopezeka pamalonda a nsomba pakati pa mayiko likuyenera kugawidwa moyenera ndi mosakondera. Maiko awonetsetse kuti katetezedwe koyenera kazachilengedwe zam'madzi kakuyenera kutsogoleredwa ndi anthu okhala m'maderawo kuti akathe kudziwa za mlingo oyenera wa nsomba zimene angaphe kuti zina zitsalekonso. . Kakonzedwe kabwino ka nsomba kakuyenera kuyamba pamene nsomba zangophedwa kumene zimene zingathandize kuchepetsa nsomba zoonongeka kotero kuchulukitsa phindu mukapita nazo kumsika.

7.9 Maiko akhazikitse ndondomeko zounikira zachilengedwe, zakhalidwe ka anthu ndi zina po wonetsetsa kuti nsomba zogulitsidwa kumisika ya kunja sizikuyika miyoyo ya anthu pachiopyezo. Pakhale kukambirana ndi magulu onse okhuzidwa pakayenedetsedwe ka malonda a nsomba m'misika yakumaiko akunja.

7.10 Maiko awonetsetse kuti magulu onse okhudzidwa ndi ntchito zing'onozing'ono za usodzi akufikiridwa ndi mauthenga okhudza malonda ansomba. Mauthengawa akuyenera kumawafikira anthu m'nthawi yake kuti akathe kupanga ziganizo zoyenera. . Maphunziro a upangiri wakakonzedwe ka nsomba ndi ulimi wa nsomba ukuyenera kufikira anthu onse okhudzidwa maka amayi ndi magulu a anthu omwe nthawi zambiri amakhala pachiopsezo komanso kuponderezedwa kuti akathe kupindula nawo malingana ndi m'mene zinthu zikuyendera kumisika padziko lonse.

8. Kusasiyanitsa kagwiridwe kantchito pakati pa amuna ndi akazi

8.1 Magulu onse akuyenera kupereka mwayi ofanana pakagwiridwe kantchito pakati pa amuna ndi akazi ndipo izi ndizotheka ngati anthuwa akugwilira ntchito limodzi. Ntchito yofananitsa m'mene amayi ndi abambo angagwilire ntchito yao ikuyenera kukhudza mbali zonse pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Njira zokwaniritsira kufananaku zikhale zosiyanasiyana potengera chikhalidwe cha anthu m'madera osiyanasiyana amene akupezeka. Izi zidzathandiza kuthetsa m'chitidwe wosala amayi.

8.2 Maiko akuyenera kutsatira zomwe zili m'malamulo ama ufulu a anthu padziko lonse. Maiko ayesetse kukwaniritsa zonse zofunika malingana ndi zimene anagwirizana mfundo zothetseratu kusalidwa kwa amayi (CEDAW) potsatira Beijing Declaration and Platform. Maiko akuyenera kutengapo mbali kulimbikitsa azimayi kumaperaka nawo ziganizo zokhudza ntchito zing'onozing'ono zausodzi. Maiko atsatire njira zapadera zothana ndi m'chitidwe osala amayi. Mabungwe omenyera ufulu apereke mpata wothandiza amayi kugwira ntchito za usodzi kudzera m'magulu awo kuti azitenga nawo mbali mzochitika zosiyanasiyana pantchito za usodzi zazing'onozing'ono. Amayi akulimbikitsidwa kutenga nawo mbali pakayendetsedwe

kamabungwe okhudza usodzi ndi zinthu zina zofunikira potukula miyoyo yawo.

8.3 Maiko akhazikitse ndondomeko ndi malamulo olimbikitsa ntchito yoti amuna ndi akazi azipatsidwa mwayi ofanana pantchito zomwe amagwira. Maiko akhazikitsenso malamulo ndi ndondomeko zolimbikitsa kusasiyana pakati pa amuna ndi akazi pa ntchito zachuma ndi chikhalidwe. Maiko akhake patsogolo zolimbikitsa kusasiyana pakati pa amuna ndi akazi. Amuna ndi akazi alembedwe ntchito ngati alangizi komanso akathe kufikiridwa mofanana pa ulangizi, ukadaulo ndi upangiri wa za usodzi. Magulu onse okhudzidwa agwilire ntchito limodzi pokonza ndondomeko, malamulo akagwiridwe kantchito, mosasala amayi.

8.4 Magulu alimbikitse ntchito zaluso zimene zingalimbikitse amayi pantchito zokhudza nsomba.

9. Ziwopsezo za ngozi ndi kusintha kwanyengo

9.1 Nkofunika kwambiri kulimbana ndizotsatira zakusintha kwa nyengo pakagwiridwe kantchito zing'onozing'ono za usodzi. , Pamafunikira kuchitapo kanthu mwamsanga potchinjiriza miyoyo ya anthu kuzotsatira za kusintha kwa nyngo zimene zimatha kusokoneza chuma ndi zachilengedwe. Ndondomeko za Bungwe la m'gwirizano wa mayiko pa kusintha kwa nyengo (UNFCCC) ndi zimene zikuyenera kumatsidwa pokonza ndondomeko zolimbana ndi kusintha kwa nyengo m'maderamu mosatayana kwambiri mfundo za Bungwe la m'gwirizano wa mayiko onse la United Nations zokhudza chitukuko.

9.2 Mbali zokhudzidwa zizindikire ndi kuganizira kusiyana kwa m'mene ntchito zing'onozing'ono za usodzi zimakhudzidwira ndi zotsatira za ngozi zogwa mwadzidzidzi, zoyambitsidwa ndi anthu komanso kusintha kwanyengo. Maiko akhazikitse ndondomeko zolimbikitsa kachitidwe kosinthika ka zinthu motsatana ndi kusintha kwa nyengo. Izi zichitike pokambirana mokwanira ndi anthu akumadera kumene kumachitika ntchito zing'onozing'ono za usodzi kuphakikizapo mzika zam'maderawo, amayi ndi magulu a anathu amene amakhala pachiopsezo nthawi zambiri komanso kuponderezedwa. Thandizo lapadera liziperekedwa kwa anthu amene amatenga nawo mbali pa ntchito zausodzi ung'onoung'ono pazilumba zingo'nozing'ono kumene kusintha kwa nyengo kutha kuwabweretsera masautso akulu pakapezedwe kachakudya, malo abwino okhala komanso kusokonekera kwa ntchito za usodzi.

9.3 Mbali zokhudzidwa zikhazikitse njira zozindikiritsa asodzi ang'onoang'ono zimene ayenera kuchita pa nthawi imene akumana ndi mavuto odza kamba ka kusintha kwa nyengo. Izi nzothandiza kulimbikitsa m'gwirizano wa zigawo zosiyanasiyana pazochitika pochepetsa mavuto odza chifukwa cha ngozi zogwa mwa dzidzidzi ndi kusintha kwa nyengo. Maiko ndi onse okhudzidwa akhazikitse njira zochepetsera kuonongeka kwa mpweya, kukololoka kwa malo am'mbali mwa nyanja mmene m'makhala zina mwa zachilengedwe zam'madzi.

9.4 Maiko aganizire zopereka thandiza kuanthu ochita usodzi ung'onoung'ono

pamene akhudzidwa ndi kusintha kwa nyengo kapena ngozi zogwa mwadzidzidzi potsira kusintha kwa nyengo ndi kuonongeka kwa zachilengedwe. Zina mwanjirazi ndi kusintha machitidwe azinthu ndikupereka thandizo la ndalama ndi zinthu zina zofunikira kwa anthu m'nthawiyi.

9.5 Ngati mavuto omwe ntchito zing'onozing'ono za usodzi zikukumana nawo ali oyambitsidwa ndi zochita za munthu, oyambitsayo apatsidwe chilango.

9.6 Mbali zonse zokhudzidwa zilingalire momwe zotsatira zakusintha kwa nyengo ndi ngozi zogwa mwadzidzi zimakhudzila gawo losamalira nsomba, malonda pa msika. Maiko azipereka thandizo ku ntchito zotukulira mausodzi ang'onoang'ono pochepetsa zotsatira zakusintha kwa nyengo. Njira zamakono zosavuta kugwiritsa ntchito zilimbikitsidwe poteteza nsomba, kakonzedwe kake komanso kulimbikitsa malonda a nsomba ku.

9.7 Maiko amvetsetse m'mene ntchito yothandiza anthu pangozi zogwa mwadzidzidzi ndi kukonzanso zinthu zimene zaonongeka imakhudziranso ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Ntchitoyi imakhudzanso mtundu wa chithandizo choyenera kuoerekedwa kwa ovutika m'nthawi yangozi zogwa mwadzidzidzi. Zitukuko zotenga nthawi yayitali zikuyenera kuganiziridwa pamene pachitika ngozi zogwa mwadzidzidzi. Thandizo loyamba pakachitika ngozi zogwa mwadzidzidzi ikhale yochepekera kwambiri kuopetsa kuvutuika kwambiri kwa anthu, kupitilira kuonongeka kwa matundu. Zinthu zimene zawonongeka zikonzedwe mwachangu potsata njira zamakono polimbana ndi kusintha kwa nyengo.

Gawo Lachitatu;
Kuonetsetsa kuti zochitika kukwaniritsidwa mwachikonzero

10. Kumveka bwino kwa ndondomeko, mogwirizana ndi kugwilira ntchito limodzi kwa mabungwe

10.1 Mayiko azindikire kufunika kogwilira ntchito limodzi pokwaniritsa ndondomeko zimene zikuoneka kuti ndizofanana monga; malamulo aboma, malamulo apadziko lonse okhudza maufulu a anthu, mfundo zokhazikitsidwa ndimaiko onse apadziko lapansi , kuphatikizapo mfundo zokhudza anthu okhala m'malo amene anabadwira, mfundo zachitukuko, mphamvu, maphunziro, umoyo ndi zina ngati; kuteteza chilengedwe, kuonetsetsa kuti chakudya chilipo chokwanira nthawi zonse, kulembana ntchito, zamalonda, zothana ndi ngozi zodza mwadzidzidzi ndi kusintha kwa nyengo, mauthenga okhudza usodzi ndi mfundo zina zokhudza malo ochitirako usodzi , kupititsa patsogolo ntchito zamalonda. Chidwi chapadera chionetsedwe posonyeza kuti palibe kusiyana pakati pa amayi ndi abambo.

10.2. Kudzera m'kafukufuku wo dziwa maganizo a anthu pazochitika, kutenga nawo mbali ndi kupereka mauthengapandondomeko ndi malamulo zokhudza kusasiyana pakati pa amuna ndi akazi pantchitzikonzedwe moyenera. Ndondomekozi zikonzedwe mogwirizana ndi mfundo za m'dera zomwe zimagwiritsidwa ntchito ndi asodzi ang'onoang'ono..

10.3 Mayiko akhazikitse mfundo zapadera poonetsetsa kuti zachilengedwe zopezeka m'madzi ndi m'nthaka zikuthandizira pokweza miyoyo ya anthu.

10.4 Mayiko aonetsetse kuti mfundo zonse zokhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi zili ndi kuthekera kothetsa njala komanso umphawi pokhulupilira kuti zachilengedwe zopezeka pa malo amodzi zimalumikizana.. Mfundo zokhudza ntchito za mausodzi ang'onoang'ono zikhale zogwirizana ndi masomphenya komanso ndondomeko zantchito ndi maufulu a anthu, kuonetsetsa kuti zikukhudza miyoyo ya anthu omwe ali pachiwopsezo choponderezedwa.

10.5 Mayiko akhazikitse ndi kulimbikitsa ubale pakati panzika zam'maiko awo, zigawo komanso dziko lonse pokwaniritsa mfundo, zoluzanitsa pakasamalidwe ka malo opezekerako nsomba. Maudindo agawidwe bwino komanso boma likhale ndi akadaulo odziwa bwino ntchito yawo kukatumikira

kumadera kumene kukuchitika ntchito zing'onozing'ono za usodzi.

10.6 Magulu okhudzidwa ndi ntchito zing'onozing'ono za usodzi alumikizane ndi akadaulo a usodzi pakapangidwe kakatundu amene atha kumakamugulitsa pamodzi monga gulu kumisika zimene zitha kuwapatitsa phindu lochulukirapo. Magulu akuyenera kumalumikizana pafupipafupi pa pogawana nzeru pakapangidwe kaziganizo zoyenera zokhudza ntchito zing'onoang'ono za usodzi.

10.7 Mayiko azindikire ndi kulimbikitsa ganizo loti ndondomeko zokhazikitsidwa m'madera ndi zothandiza kwambiri makayendetsedwe kamalo amene kumachitikira ntchito za usodzi ung'onoung'ono mogwirizana ndi zolinga zosamalira chilengedwe chomwe chiri chodalirana.

10.8 Mayiko alimbikitse m'gwirizano pakati pawo poteteza ntchito za usodzi ung'onoung'ono. Mayiko komanso nthambi zokhudzidwa zithandize kupereka maphunziro kuti anthu amvetsetse zokhudza ntchito zing'onozing'ono za usodzi komanso kuthandiza pazinthu zofunika mayiko monga ntchito zamtengatenga.

11. Kufalitsa mauthenga, zotsatira zakafukufuku ndi kulumikizana

11.1 Mayiko akhazikitse ndondomeko zofalitsira mauthenga ndi zotsatira zokhudza kafukufuku wansomba, kusamalira zachilengedwe kuphatikizapo umoyo, zachuma, chikhalidwe cha anthu m'madera amene kumachitika usodzi ung'ono ung'ono zimene zili zofunika popanga ziganizo zokhudza njira zamakono ndi zokhazikika zokhudza usodzi ndi kasamalidwe kachilengedwe. Ndondomeko zikhazikitsidwe mosakondera amuna kapena akazi. Pakhale mauthenga omveka otsindika zaubwino wantchito za usodzi zing'onozing'ono pachuma ndi kuthandizira moyoyo ya anthu.

11.2 Onse okhudzidwa kumadera komwe kumachitikira ntchito za usodzi zing'onozong'ono azindikire kulumikizana kwa zachilengedwe ndi kufunika kwa mauthenga akamapanga ziganizo zoyenera.

11.3 Mayiko ayesetse kupewa katangale makamaka popititsa patsogolo chilungamo, kuonetsetsa kuti adindo akugwira ntchito moyenera komanso kuti sipakukhala ziganizo zokondera kapena kupondeleza anthu okhala m'malo amene mumachitika ncthito zing'onozing'ono zausodzi.

11.4 Magulu onse okhudzidwa azindikire kuti anthu akumadera amene kumagwiridwa ntchito za usodzi ung'ono ung'ono ali ndi udindo ofikiridwa ndi uphungu oyenera. Ndikofunika kumvetsetsa kufunika kopeza mauthenga abwino m'nthawi yake maka kwa anthu okhala m'madera kumene kumachitika ntchito zing'onozong'ono za usodzi. Mabungwe azithandizapo pakagwa ngozi zadzidzidzi kamba ka kusintha kwa nynego kapoena kusakazika kwachilengedwe komanso anthu

okhudzidwa akuyenera kuthandizidwa kuti akathe kudzukanso ndi kuchita ta bwino pamiyoyo yawo. Mauthenga akuyenera kukonzedwa malingana ndi chiopyezo chimene chingafikire dera ntchito zachuma, malamulo okhazikika , komanso chikhalidwe cha anthu pantchito za usodzi.

11.5 Mayiko awonetsetse kuti akuoereka mauthenga oyenera kuti ntchito zausodzi zing'onozongono zikugwiridwa mwadongosolo motsata osatsata malamulo. Ntchitozi zikhudzenso kuopsya kwa mavuto ogwa mwadzidzidzi, kusintha kwa nyengo, umoyo ndikulimbikitsa kapezekedwe kachakudya mosaiwalanso magulu a anthu amene atha oponderezedwa mosavuta. Ndondomeko za mauthenga zikonzedwe panyengo zovuta.

11.6 Magulu onse okhudzidwa awonetsetse kuti anthu akumadera kumene anthu akuchita usodzi ung'ono ung'ono akuidziwitsidwa paza chikhalidwe, zikhulupiliro zawo.Anthuwa akuyenera kuthandizira ntchito zzachitukuko kumadera awo. Maganizo operekedwa ndi acmayi amene amagwira nawo ntchito za usodzi akuyenera kulingalilidwa pakakonzedwe kandondomeko zantchito. Mayiko asonkhanitse pamodzi maluso achimakolo okhudza za usodzi amene amachitika m'madera m'mene m'machitikra ntchito zing'onozing'ono za usodzi. Izi zidzathandiza kudziwa momwe usodzi umachitikira mzaka mam'buyomu ndi m'mene wasinthiranso masiku ano potsindika katetezedwe kazachilengedwe..

11.7 Mayiko ndi mabungwe okhudzidwa apereke thandizo la ndalama ndi upangiri wabwino kwa anthu okhala m'madera amene kukuchitika ntchito zing'onozing'ono za usodzi maka kwa amayi kuti ziwathandizire kukonza ndondomeko zopititsa patsogolo usodzi wawo ndi ulimi wansomba.

11.8 Magulu alimbikitse kafalitsidwe ka mauthenga maiko onse okhudza ulimi wansomba pogwiritsa ntchito zipangizo ndi ukadaulo wamakono. Mauthengawa akueyenera kufalitsidwa moganizira chikhalidwe cha anthu, maufulu awo komanso malamulo okhazikika aboma ndi mabungwe. Mauthengawa athandizire kubweretsa chitukuko m'madera m'mene mumachitita ntchito zing'onozing'ono za usodzi, komanso athandize kuluzanitsa anthu . Moganizira za moyo wa anthu watsiku ndi tsiku, chikhalidwe komanso njira zofalitsira, mauthenga aperekedwe m'njira yoti ukathe kufikira anthu m'njira yoti ukathe kuluzanitsa anthu ndi kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito kaluso pakati pa anthu pa nchito zing'onozing'ono za usodzi.

11.9 Mayiko ndi magulu ena okhudzidwa awonetsetse kuti payikidwa ndalama zokwanira zochitira kafukufuku wa ntchito zing'onozing'ono za usodzi ndipo akuyenera kutengapo mbali. Kafukuku okhudza ntchito zausodzi akuyenera kuchitika mogwirizana pakati pa maiko ndipo zotsatira

zake zithandizire dwe popanga ziganizo zoyenera pantchito zawo. Mabungwe ndi nthambi zafukufuku zithandize kupereka maphunziro olora madera antchito zing'onozing'ono za usodzi kutenga nawo mbali pakafukufuku ndi kagwiritsidwe ntchito kazotsatira zake. Zolinga zakafukufuku zikhale zogwirizana poyang'ana gawo lomwe ntchito zing'ono zing'ono zausodzi zimathandiza pakapangidwe kazipangizo kokhalitsa, kapezekedwe kazakudya, komanso kuthana ndi umphawi. Zfufuzidwa zikonzedwe pokambirana kaye ndi anthu kapena mabungwe amene akuonetsa chdwi pa ntchito zing'onozing'ono za usodzi..

11.10 Mayiko ndi magulu okhudzidwa alimbikitse kafukufuku wokhudza kagwiridwe kantchito kuphatikizapo nzika zochoka kumaiko ena. Mwa zina patha kuchitika kafukufuku pa umoyo, maphunziro, ubale pakati pa amayi ndi abambo. Izi zingathandizire kupanga ndondomeko zolimbikitsa kagwiridwe kantchito mofanana pakati pa amayi ndi abambo mu usodzi. Ntchito yolimbikitsa kuti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo ichitike motsatana ndi kafukufuku pamene mfundo zokhudza chitukuko cha madera kumene kukuchitika usodzi ung'onoung'ono. Izizidzathandiza kupeza polowera posafuna kusiyanitsa pakati pa amayi ndi abambo pakagwiridwe ka ntchito. Akalozera osonyeza kayendetsedwe ka ntchito yokhudza kusiyana pakati pa amayi ndi abambo agwiritsidwe ntchito poyang'ana ndi kukonzanso mavuto obwera chifukwa cha kusiyana pakati pa amayi ndi abambo. Ndondomekozi zidzathandiza zkusintha khalidwe la anthu.

11.11 Kuzindikira kufunika kwa malo ochitirako usodzi ung'onoung'ono, mayiko ndi magulu okhudzidwa alimbikitse maphunziro opititsa patsogolo kasamalidwe kachilengedwe cham'madzi ndi m'mene chingathandizire pachitukuko monga thanzi lobwera podya nsomba. Mauthenga othandiza kudziwitsa anthu zaubwino wa nsomba afalitsidwe.

12. Kupereka upangiri

12.1 Mayiko ndi magulu okhudzidwa athandize anthu ogwira ntchito zing'onozing'ono za usodzi powapatsa upangiri umene ungawathandize kutenga nawo gawo popanga ziganizo zokhudza ntchitoyi. Kuti izi zitheke mpofunika kuwonetsetsa kuti onse amene amatenga nawo gawo pantchito zing'onozing'ono za usodzi akudziwa bwino zomwe zimachititsa kuti nsomba zikapezeke ku msika. Izi zizichitika mwadongosolo lokhazikika mwamalamulo odziwika ndi ovemerezedwa ndi onse. Chidwi chipite kuntchito yoonetsetsa kuti amayi akukhala nawo m'maudindo okhazikika pakayendetsedwe kantchito za usodzi m'madera awo..

12.2 Mayiko ndi magulu okhudzidwa apereke uphungu ndi upangiri kwa ogwira ntchito zing'onozing'ono za

usodzi. Mwachitsanzo; Kudzera m'ntchito zachitukuko, polora ntchito zing'onozing'ono zausodzi kukhala zaphindu, kulimbikitsa mwayi wochita malonda a nsomba.

12.3 Magulu onse okhudzidwa azindikire kuti maphunziro ali ndi kuthekera kopereka upangiri umene umawonjezera nzeru ndi luso latsopano. Izi ziyenera kuchitika mopereka mpata oti ophunzitsa akathe kuphunzira zina ndi zina kuchokera kwa ophunzitsa, ndipo maphunzirowa achitike mogwiritsa ntchito njira zosavuta pokwaniritsa zosowa za anthu kuphatikizapo amayi ndi abambo komanso anthu amene moyo wawo nthawi zambiri umakhala pachiopyezo kapena kuponderezedwa kumene.Ntchito yopereka upangiri imafunika kuthandiza anthu kuti adzipeza njira zolimbanirana ndi mavuto omwe angamakumane nawo kudera kwawo posintha machitidwe awo azinthu.

12.4 Nthambi zaboma zigwire ntchito yobweretsa kusintha kudzera m'maluso osiyanasiyana polimbikitsira ntchito zing'onozingo'no za usodzi zokhalitsa. Nthambi zaboma zomwe zili ndi mphanvu zopanga ziganizo pazokha komanso zimakhudzidwa ndi ntchito za usodzi zikueyenera kuonetsa chidwi chapadera pomakonza malamulo olimbikitsa chitukuko ndi ulamuliro wabwino m'madera amene mumachitika ntchito zing'onozing'ono. Alimbikitsenso ntchito zakafukufuku.

13. Thandizo pokwaniritsa ndondomeko ndi kulondoloza kakwaniritsidwe kake

13.1 Magulu onse okhudzidwa akulimbikitsidwa kukwaniritsa ndondomekozi mogwirizana ndi zomwe boma likufuna kuchita m'dziko.

13.2 Mayiko ndi magulu onse okhudzidwa agwiritse bwino ntchito thandizo chuma. Mayiko ndi mabungwe othandiza pachitukuko m'mayiko otukuka kumeneakuyenera kuthandiza mayiko onse apadziko la pansi pantchito yolimbikitsa kukhazikitsa ndondomeko, zolimbikitsa m'ngwirizano pakati pawo. Thandizo litha kukhala nzeru kapena zipangizo zothandizira pachitukuko chadziko pachuma, kukonza malo ogwilira ntchito, kugawana nzeru ndi maupangiri ena, kukonza ndondomeko zoyendetsera ntchito zing'onozing'ono zausodzi m'dziko. Luso lapamwba liperekedwe kwa amene akulisowa.

13.3 Mayiko ndi magulu okhudzidwa agwire ntchito pamodzi pofuna kudziwitsa anthu zandondomekozi komanso kufalitsa uthenga omasulilidwa bwino m'zilankhulo zina pofuna kupindulira ogwira ntchito zingo'nozingono zausodzi. Mayiko ndi mabungwe okhudzidwa akhazikitse mfundo ndi ndondomeko zapadera zochepetsa kusasiyana pakati pa amayi ndi abambo kuti akathe kumagwilira

ntchito limodzi gawana za usodzi zingo'nozing'ono potukula miyoyo ya amayi.

13.4 Mayiko azindikire kufunika kwa ndondomekozi ndipo awonetsetse kuti zikulondolozedwa pokwaniritsa zolinga zake. Pakhalenso kauniuni ofuna kudziwa momwe anthu akuchitira ndi maufulu okhala ndi chakudya ngati mbali imodzi ya udindo wa dziko lawo owonetsetsa kutianthu ali ndi chakudya chokwanira m'dziko komanso ntchito yothetsa umphawi. Pakuyenera kukhala ndondomeko zothandizira kuti zotsatira zafukufuku zidzigwiritsidwa ntchito pokonza mfundo zotsogolera zochitika zam'dziko. Kusiyana pakati pa amayi ndi abambo kuziganziridwa mwapadera powonetsetsa kuti zikutsatidwa moyenera zomwe zingathadize kuti kutukula miyoyo yaamayi. Mayiko ndi magulu okhudzidwa afotokoze momveka bwino njira zimene anthu atha kutsatira potukula ntchito za usodzi zing'onozing'ono. Afotokonzenso momwe amayi ndi abambo angamatengale nawo mbali posamalira zachilengedwe kuti padzikhala chakudya chokwanira ndi kuthetsa umphawi.

13.5. Mayiko atsogolere zochitika m'ma iko awo pakakwaniritsidwe ka ndondomekozi. Awonetsetsenso kuti magulu oyimira magawo osiyanasiyana m'dzikomo makama omeneyera maufulu achibadwidwe akutenga nawo mbali pantchitoyi. Anthu ogwira ntchito zing'onozing'ono za usodzi akangalike pokwaniritsa njira zakuya kuti zikugwiritsidwadi ntchito pokwaniritsa ndondomekozi.

13.6 Bungwe la FAO lilimbikitse ndi kuthandiza kukhazikitsidwa kwa ndondomeko ya Global Assistance Programme yokhala ndi mapulani m'zigawo zogwilira ntchito zothandizira kukhazikitsidwa kwa ndondomekozi.

Ndondomeko zosakakamiza zolimbikitsa ntchito zing'onozing'zono za usodzi wokhalitsa zogwirizana ndi ntchito yowonetsetsa kuti anthu ali ndi chakudya chokwanira ndi kuthetsa umphawi zakonzedwa kuti zithandizire mfundo zoonesetsera kuti ntchito zokhudza nsomba zikugwiridwa potsatira mfundo zabwino zomwe zinakhazikikitsidwa m'chaka cha 1995 ndi bungwe la FAO. Ndondomekozi zinakonzedwa kuti zipereka chitsogozo chothangatira ntchito zing'onozing'ono za usodzi polimbikitsa mfundozi zimene zinakhazikika ndi zinthu zonse zotsatira Ndondomekozi zinakonzedwa kuti zithandizire kupititsa patsogolo kufunikira kwa ntchito zing'onozing'ono za usodzi, kotero nthu athe kuzizindikira, kulimbikitsa komanso kuti zithandizire kuthetsa njala ndi umphawi padziko lonse. Ndondomekozi zikulimbikitsa ntchito zausodzi zogwiridwa motsatana ndi chitukuko chokhalitsa pa miyoyo ya anthu ndi kapezedwe ka chuma chopindulira m'badwo uno ndi mibadwo yamtsogolo, moganizira asodzi ang'onoang'ono ndi anthu amene amagwira ntchito zing'onozing'ono zokhudza nsomba komanso ntchito zina zokhudza usodziwu komanso gulu la anthu amene miyoyo yawo imakumana ndi ziopsezo zosiyanasiyana kawiri kawiri.

ISBN 978-92-5-135848-1
I4356NY/1/03.22